# MPINJI ZONE EXAMINATIONS BOARD

**2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

**(100 Marks)**

**Date:** 29/02/2024 **Time Allowed:** 13:00 – 15:15 ($2\frac{1}{4}$ $hrs$)

**Name of Candidate :** ______________________________________________
**(Surname First)**

**Name of School :** ______________________________________________

**Instructions**

1. Onetsetsani kuti pepalali liri ndi masamba asanu ndi atatu
2. Lembani dzina lanu ndi la sukulu yanu pamwambapo
3. Pepalali liri ndi magawo anayi
4. Tsatani malangizo m'magawo onse
5. Chonga mu bokosili mafunso onse omwe mwayankha

| Question Number | Tick if answered | Do not write in this column | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 7 - 46 | | | |

## GAWO A: MALIKISI 30

Yankhani funso limodzi lokha basi mu gawoli. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150**.

1. Lembani chimangirizo pa mutu woti "Mzanga wa pamtima". Mwa zina tsatani izi polemba.

**Ndime yoyamba**
- Dzina la mzanuyo
- Komwe amakhala
- Maonekedwe ake

**Ndime yachiwiri**
- Zomwe iye amakonda kuchita
- Zomwe mukuchita pofuna kulimbikitsa ubwenzi wanu

**Ndime yachitatu**
- Ubwino womwe mwaona pokhala ndi mzanu wa pamtimayo

**KAPENA**

2. Yerekezani kuti mwasankhidwa kukayamba folomu 1 ku Luchenza sekondale sukulu koma simunapite msanga chifukwa mukudwa. Lembani kalata kwa mphunzitsi wamkulu wa Luchenza sekondale sukulu P. O. Box 84, Luchenza yomudziwitsa za kudwala kwanu. Mwa zina tsatani izi polemba.

**Ndime yoyamba**
- Cholinga cha kalata
- Ndinu mnyamata kapena msungwana
- Komwe munkaphunzira

**Ndime yachiwiri**
- Matenda omwe mukudwala
- Nthawi yomwe mudayamba kudwala matendawo
- Zomwe mukuchita kuti muchire
- Mukuyembekezera kufika liti ku sukulu

**Ndime yachitatu**
- Zomwe muzachite kusukuluko posonyeza kuti mwayamba mochedwa.

**Poyankhira**

## GAWO B: MALIKISI 20

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenako muyankhe mafunso otsatirawo.

Atangolowa m'kalasi tidaziwiratu kuti madzi achita katondo, popeza mbiri ya mwamuna wa mayiyu ndi Nyadani idali yaiwisi. Mphunzitsi wamkulu wa sukulu ya Khombedza adayetsetsa kumuchenjeza koma iye adatemetsa nkhwangwa pa mwala. Iye ankati adafa bulu. Zakuti kunja kuno kuli matenda ankangoziponya ku chikuto namati: kaya, zanu, ine bola zanga zikuyenda.

Aliyense ankamulangiza ankamutenga ngati mdani wake popeza adali ngati omutsekera njira kutsogolo kwake. Dzidzidzi mayi wina adangoti lowu mu sitandade 8 atamangisira chitenje chake m'mimba, nalunjika padakhala Nyadani ndi Mbeyani mnyamata wa zitho. Iye adafuna kuchita za nthanthi zake koma adazindikira nkhwangwa ili m'mutu. Pomwepo adathawa ndipo adazindikira kuti kalulu akabisala pa chitsamba amapha ndi chitsamba chomwecho.

"Ndikufuna iweyo, Nyadaniwe. Lero undimva madzi. Undiuze kumene kuli mwamuna wanga," Anatero Nachithizi akupumira m'mwamba. Tonse tidakuza bwalo kuti tionere zigogodo. Zidali zamanyazi kuona awiriwa akutuwitsana ngati akapoli. Siketi zidagawukira uko, ena nkumagula malondaa aulere.

Nyadani adali mtsikana wokongola mogometsa mafuko. Kwawo kudali ku Namtombozi kuseli kwa phiri la Nampini. Makolo ake adali opembedza. Iwo adayetsetsa kumulangiza koma pakuti m'mimba ndi m'chipala, Nyadani adapatuka. Bambo ake akumwalira adamusira mawu nati, mwanawe ndiwe kholo la alongp akowa. Chonde dekha kuti uzavale mkanda woyera.

Mwambo wa maliro utatha Nyadani adabwerera ku sukulu ndipo ankakhozadi. Koma ndalama ndi zimene zinkamuvuta zimene zidamchititsa kuti azisirira ndi kumakasakasaka makwacha kuti amalize sukulu.

**Mafunso**

a. Kodi Nyadani adali kalasi yanji?

________________________________________ **(malikisi 1)**

b. Kwawo kudali kuti?

________________________________________ **(malikisi 1)**

c. Fotokozani za khalidwe la Nyadani.

________________________________________ **(malikisi 2)**

d. N'chifukwa chiyani adayamba khalidwe limeneli?

________________________________________ **(malikisi 2)**

e. Tchulani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa omwe apezeka mu nkhaniyi:

i. Mphamvu ________________________________ **(malikisi 1)**

ii. gomo ________________________________ **(malikisi 1)**

f. Fotokozani tanthauzo la mkuluwiko woti "kalulu akabisala pa chitsamba amapha n'chisamba chomwecho".

________________________________________ **(malikisi 2)**

g. N'chifukwa chiyani ophunzira adakuza bwalo?

________________________________________ **(malikisi 1)**

h. Lembani chifanifani chomwe chikupezeka mu nkhaniyi.

________________________________________ **(malikisi 2)**

i. Tchulani malonda aulere omwe ophunzira adagula pa tsikuli.
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 2)**

j. Kodi kutemetsa nkhwangwa pa mwala n'kutani?
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

k. Tchulani mawu amene abambo ake adamisiyira asanamwalire.
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 2)**

l. Lembani mawu omwe akutsimikiza kuti Nyadani adali woyamba kubadwa.
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 2)**

## GAWO C: MALIKISI 10

4. Werengani kankhani kotsatiraka kenako muyankhe mafunso otsatirawo

Kodi Mgwagwa, ndaona ine chaka chino ndi izo basitu ine mtsuko wanga tengu. Mwana kumbuyoku ikeni, ndisiye Liheyu akukazinga chimanga cha mbuliuli. Ndiye kuti atsire mafuta basi chimoto lawi. Ndiyetu kumaso konseku kutheratu. Mmene ndimafika, ine kungodabwira fungo. Nditere basi mwana kulibe a mfumu. Mtengo wagwa nanga nthyole kuti ndiwo?

**Mafunso**

i. Kodi ndi malonje anji amenwa?
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

ii. Kodi akuyankhula m'nkhaniyi ndani?
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

iii. Chachitika ndi chiyani m'nkhaniyi?
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

iv. Fotokozani tanthauzo la mkuluwiko woti "nthyole kuti ndiwo".
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

v. Kodi n'chifukwa chiyani oyenda pansi pa msewu amayenda kumanja?
_______________________________________________________________________________ **(malikisi 1)**

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu otsatirawa.

a. nzime
_______________________________________________________________________________

b. lowu
_______________________________________________________________________________

c. lubza
_______________________________________________________________________________

d. tsamba
_______________________________________________________________________________

e. bwino
_______________________________________________________________________________

## GAWO D: MALIKISI 40

Sankhani **mitundu ya mawu** atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

6. Elube <u>wapita</u> kale ku msika.

A. dzina
B. mneni
C. mperekezi
D. muonjezi

7. Tayenda mofulumira <u>zedi</u>.
   A. mneni
   B. muonjezi
   C. mfotokozi
   D. mvekero

8. Kukhala osauka <u>si</u> tchimo.
   A. maonjezi
   B. dzina
   C. mneni
   D. mfuwu

9. <u>Gobede</u>! Zonse zili pansi.
   A. mvekero
   B. mfuwu
   C. dzina
   D. mneni

10. Awabera katundu <u>wawo</u> dzulo.
   A. dzina
   B. mfotokozi
   C. mlowammalo
   D. mvekero

Sankhani chiganizo chomwe chili ndi **zizindikiro zoyenera** za mkalembedwe m'ziganizo zotsatirazi.

11.
   A. wati ndimutenge komabe ndiganize kaye.
   B. Wati ndimutenge; komabe ndiganize kaye
   C. wati ndimutenge;  komabe ndiganize kaye.
   D. Wati ndimutenge; komabe ndiganize kaye.

12.
   A. Zuze, chirombo cha m'mudzi, waphedwa lero.
   B. Zuze chirombo cha m'mudzi, waphedwa lero.
   C. Zuze chilombo cha m'mudzi waphedwa lero.
   D. Zuze, chirombo cha mmudzi waphedwa lero

13.
   A. John adati, Tiwonge asabwere nawo.
   B. John adati, Tiwonge asabwere nawo
   C. John adati, "Tiwonge asabwere nawo".
   D. John adati, "Tiwonge asabwere nawo"

14.
   A. Kalanga ine.
   B. Kalanga, ine!
   C. Kalanga ine!
   D. Kalanga! ine.

15.
   A. Lero taphunzira, "Aneni"
   B. Lero taphunzira, Aneni.
   C. Lero taphunzira "Aneni"
   D. Lero taphunzira aneni.

Sankhani mitundu ya **misintho ya aneni** omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

16. Kapu yanga <u>idasweka</u>.
   A. wom'chitira
   B. wam'chibisira
   C. wochitidwa
   D. wochititsa

17. Mwana uja <u>wamenywa</u>.
   A. wonyazitsa
   B. womchitira
   C. wochitirana
   D. wochitidwa

18. Agogo <u>amasula</u> galu uja.
   A. wochitirana
   B. wochitidwa
   C. wochititsitsa
   D. wamtsutso

19. Njinga zija <u>zaombana</u>.
   A. wochititsitsa
   B. wochitirana
   C. wochititsa
   D. wochitidwa

20. Agogo <u>amagonagona</u>.
   A. wobwerezabwereza
   B. wotsutsa
   C. wochitidwa
   D. wochititsitsa

Sankhani **magulu a mayina** omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

21. Iye ndi <u>kaziotche</u>.
   A. Mu – Mi
   B. Ka – Ti
   C. U – Ma
   D. Mu – A

22. Sungeni adali <u>chumba</u>.
   A. U – Ma
   B. Mu – A
   C. Mu – Mi
   D. Chi – Zi

23. <u>Kumwa</u> madzi n'kofunika
   A. Ka – Ti
   B. Li – Ma
   C. Ku + Tsinde la mneni mwa
   D. Mu – Mi

24. <u>Sukulu</u> yathu ndi yokongola.
   A. Li – Ma
   B. Chi – Zi
   C. U – Ma
   D. I – Zi

25. <u>Makolo</u> ake abwera.
   A. Mu – Mi
   B. Li – Ma
   C. I – Zi
   D. Chi – Zi

Sankhani **mvekero** woyenera kukhala m'mipata ya ziganizo zotsatirazi.

26. Wafika mbandakucha kuli __________
   A. mbu
   B. mbe
   C. bi
   D. psu

27. Mbavayo idangoti _______ kusowa chonena.
   A. jenkha
   B. yasa
   C. zi
   D. phi

28. Tadala ali ______ pakhonde.
   A. zi
   B. fwa
   C. khuma
   D. nji

29. Pamudzi panali __________
   A. ndwi
   B. zi
   C. mbu
   D. phe

30. Mkango udangoti _______
   A. fwanthu
   B. deru
   C. mbwe
   D. balamanthu

Sankhani **matanthauzo a zining'a** zotsatirazi.

31. Gunda njovu.
   A. khala wosabala
   B. khala pansi
   C. khala chete
   D. khala pampando

32. Lowa pansi.
   A. mwalira
   B. sauka
   C. chita mantha
   D. chita manyazi

33. Kola chona.
   A. ipha nyama
   B. chita ulenje
   C. mwalira
   D. palamula

34. Ponda njati.
   A. sauka
   B. lemera
   C. tenga matenda opatsirana pogonana

D. khala ndi mimba

35. Kumaso
    A. kutsogolo
    B. maliseche
    C. kumbuyo
    D. kumanda

Sankhani mayina omwe ali m'mitundu yotsatirayi.

36. Dzina lopanda mwinimwini.
    A. ulesi
    B. mulu
    C. shire
    D. nyakwawa

37. Dzina launyinji.
    A. phava
    B. uve
    C. anyamata
    D. malingaliro

38. Dzina lamwinimwini.
    A. nthungo
    B. matumbo
    C. zomba
    D. sukulu

39. Dzina la chinthu chokhudzika.
    A. ulesi
    B. ulemu
    C. mlengalenga
    D. mpando

40. Dzina la chinthu chosakhudzika.
    A. mbatata
    B. tsoka
    C. munthu
    D. malovu

Sankhani mitundu ya **nthambi za ziganizo zosaima pozokha** zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

41. Ophunzira <u>omwe azakhoze bwino</u> azawasankhira ku sekondale.
    A. ya mfotokozi
    B. yoyima payokha
    C. ya muonjezi
    D. ya dzina

42. Mvula ivuta kubwera <u>chifukwa tadula mitengo yonse</u>.
    A. ya dzina
    B. ya mfotokozi
    C. yoyima payokha
    D. ya muonjezi

43. <u>Zoti nyanja yathu ikuphwa</u> ndizoona.
    A. ya muonjezi
    B. yoima payokha
    C. ya mfotokozi
    D. ya dzina

44. Mnyamata <u>amene wakhala apoyo</u> ndi wakuba.
    A. yoyima payokha
    B. ya dzina
    C. ya mfotokozi
    D. ya muonjezi

45. Uzapambana <u>pokhapokha ukazalimbikira</u>.
    A. ya muonjezi
    B. yoyima payokha
    C. ya mfotokozi
    D. ya dzina

# MAFUNSO ATHERA PAMENEPA